EXAMINATION **NO.:** ____________

# NSENJERE ZONE EXAMINATIONS BOARD

**2022 PRIMARY SCHOOL LEAVING CERTIFICATE MOCK EXAMINATIONS**

# CHICHEWA

**(100MARKS)**

**Subject Number: P032**

**Time Allowed: $2\frac{1}{4}$ hours**

**Friday, 5th May, 2022** **1:00 – 3:15 pm**

**Dzina lanu: ________________________________**

(kuyamba ndi labambo)

**Dzina la sukulu yanu ____________________________________**

**MALANGIZO**

1. Onetsetsani kuti pepala ili lili ndi **masamba** khumi
2. Pepala lili ndi magawo **anayi**: Gawo **A**, **B**, **C** ndi **D**
3. Lembani **dzina lanu** ndi **dzina la sukulu yanu** pamwamba pa tsamba lino
4. Lembani **nambala ya mayeso** pamwamba pa tsamba lililonse
5. Lembani **chimangilizo** kapena **kalata** mu Gawo **A**, ndipo yankhani mafunso onse mu Gawo **B**, **C** ndi **D**
6. Lembani yankho lanu mu Gawo **A** pa pepala lomwe lili kumathero kwa mafunso a mugawoli.
7. Yankhani mafunso **onse** a mu Gawo **B** ndi **C** mmipata yomwe yaperekedwa pansi pa funso lililonse
8. Yankhani mafunso a mu **Gawo D** pozunguliza lembo lokhoza pafunso lililonse
9. Muchitebulo chili pamwambachi onetsani funso lililonse lomwe mwayankha **pochonga** mubokosi lomwe lili kutsogolo kwake
10. Perekani kwa **oyang'anira mayeso** (imvijireta)pepala lonseli nthawi ikakwana

| **Funso** | **Chongani zomwe mwayankha** | **Muno musalembemo** | |
|---|---|---|---|
| **1** | | | |
| **2** | | | |
| **3** | | | |
| **4** | | | |
| **5** | | | |
| **6 - 10** | | | |
| **11 - 15** | | | |
| **16 - 20** | | | |
| **21 - 25** | | | |
| **26 -30** | | | |
| **31 - 35** | | | |
| **36 -40** | | | |
| **41 - 45** | | | |
| | | | |

## GAWO A (malikisi 30)

**Langizo,** yankhani funso limodzi lokha mwa mafunso awiri ali m'munsiwa. Sankhani mutu wa chimangirizo kapena kalata. Mau a chimangirizo chanu kapena kalata yanu asachepere 100 koma sabzole 150

1. Lembani chimangirizo pa mutu uwu:
   UBWINO WOSAMALIRA KATUNDU WA SUKULU

Mwa zina tsatirani izi polemba :

**Ndime yoyamba**

- Katundu yemwe ali pa sukulu panu
- Momwe sukulu yanu idamupezera katunduyo
- Omwe amasamalira katunduyo

**Ndime ya chiwiri**

- Zomwe zimachitika posamalira katunduyo
- Ubwino osamalira katunduyo

**Ndime yachitatu**

- Kuipa kosasamalira katundu wa sukulu

**KAPENA**

2. Lembani kalata kwa phungu wa nyumba ya malamulo woyimira dera lanu, Bokosi 7340, Chikwawa, kuti akakupemphereni ku Boma msewu waphula m'dera lanu.

Mwa zina tsatani izi polemba kalata yanu:

**Ndime yoyamba**

- Dzina la msewu
- Kumene msewuwo ukupita
- Kutalika kwa msewuwo

**Ndime yachiwiri**

- M'mene msewuwo ulili panopa
- Mavuto amene akuchitika chifukwa cha msewuwo
- Zomwe boma lingachite pavuto lamsewuwo

**Ndime ya chitatu**

- Kuthandiza kwa msewuwo ukadzakonzedwa

## GAWO B (malikisi 20)
## KUMVETSA NKHANI

3. Werengani nkhani yotsatirayi mosamala kwambiri kenaka yankhani mfunso otsatirawo:

Kulera ana sikungowayang’anira kuti akudya kapena kuvala bwino ayi. Panafunika kuwalangiza kuti akule ndi makhalidwe amene angawathandize pamoyo wawo wonse, popeza iwowa ndi atsogoleri a mawa. Nawonso ayenera kudzathandiza ana awo m’tsogolo muno.

Kawirikawiri ana amaphunzira bwino ndi zitsanzo osati ndi mawu okha. Ngati tiwuza ana kuti adzifika pakhomo dzuwa lisanalowe pafunika kuti tionetse kuti ifenso makolo tidzifika pakhomo nthawi yabwino. Ngati makolo awuza ana kuti asamwe mowa kapena asasute fodya, aonetsetse kuti iwowo sakuchita izi chifukwa ndi chinthu chosamveka kwa mwana kuti asachite zoterozo pamene akuona makolo akuchita zomwezo.

Sibwino kumuopseza mwana amene walakwa pomuuza zomwe sangachite, monga kuti ndidzakupha pamene tikufuna kuti asinthe chifukwa amazindikira kuti ndizonama. Choncho iye amapepusa malangizo operekedwawo. Ngati mwana walakwa tiyeni timulange nthawi yomweyo ndipo moyenera.

Mwana akalakwa pakhomo, abambo ena amakalipira amayi amvekere, “Taona zimene mwana wakoyu akuchita!” Kwenikweni akalakwa chachikulu ndiye amati, “choka pakhomo pano pamodzi ndi mwana wakoyi!” kodi wasanduka mwana wa mayi yekha chifukwa walakwa?

Makolo enanso sadziwa kulanga ana monga m’mene ayenera kuchitira. Ena ngakhale mwana alakwe chotani , sakalipa ayi, amangoyang’ana. Kodi zimenezi zibzala chiyani mwa mwanayo? Chofunika ndi chakuti makolo asonyeze udindo wawo polanga ana akalakwa chifukwa akapanda kutero anawo sakula ndi makhalidwe abwino.

Pamene mwana walakwa muitaneni ndikumudzudzula nthawi yomweyo. Muthanso kumukwapula ndi ka chikwapu kakang’ono osati chindodo chachikulu ayi. Zimenezi ziyenera kuchitika nthawi yomweyo imene mwanayo walakwa. Pamenepa mwana amazindikira kuti akulangidwa chifukwa cha zomwe walakwa. Ana ena okulirapo ayenera adzudzulidwe paokha osati pamene pali ana ang’ono. Koma tikangoyang’ana amaganiza kuti kukhala ndikumeneku.

Tiyeni tidzudzule pakaoneka cholakwa osangoyang'ana popeza muvi woyang'anira suchedwa kulowa m'maso.

Pali ana ena omwe ndi ankhutukumve, amangokhala ngati adalodzedwa. Ngakhale alangizidwe iwo amangobwerezabe zolakwazo. Ana otere tisatope nawo koma tiyenera kuwalangizabe chifukwa ngakhale avute ali m'manja mwathu.

Tsopano yankhani mafunso otsatirawa pa mizere ili pansi pa funso lililonse.

(a) Kodi atsogoleri a mawa ndani?

____________________________________________________________( malikisi 1)

(b) N'chifukwa chiyani atsogoleri a mawa ayenera kulangizidwa?

______________________________________________________________________

____________________________________________________________(malikisi 2)

(c) Perekani zitsanzo ziwiri zomwe makolo angachite poonetsa makhalidwe abwino?

______________________________________________________________________

____________________________________________________________(malikisi2)

(d) N'chifukwa chiyani makolo ayenera kuphunzitsa ana ndi zitsanzo pakhomo osati ndi mawu okha?

______________________________________________________________________

____________________________________________________________(malikisi 2)

(e) Kodi mwana amadziwa bwanji kuti zimene akumulangiza n'zonama?

____________________________________________________________(malikisi 1)

(f) Ndi mavuto **awiri** ati omwe amayi amatha kukumana nawo mwana akalakwa?

______________________________________________________________________

____________________________________________________________(malikisi2)

(g) Kodi mwini wa ana pakhomo ndani?

____________________________________________________________(malikisi 1)

(h) N'chifukwa chiyani ana ena sakula ndi makhalidwe abwino?

______________________________________________________________________

____________________________________________________________(malikisi 2)

(i) Kodi ndi nthawi yanji yomwe mwana ayenera kulangizidwa akalakwa?

____________________________________________________________(malikisi 1)

(j) Pezani mawu m'nkhaniyi omwe akutanthauza

(I) **"ana osamva"**

______________________________________________________(malikisi 1)

**(II) "kungokhala osachita kanthu"**

______________________________________________________(malikisi 1)

(k) Kodi makolo ayenera kuchita chiyani ngati ana akupitirizabe kulakwa?

____________________________________________________________

____________________________________________________(malikisi 2)

(l) Perekani mutu wa nkhaniyi

____________________________________________________(malikisi 2)

## GAWO C (malikisi 10)

4. Werengani kankhanika ndipo muyankhe mafunso otsatirawa.

Nabetha : Odii kuno.

Nanyoni : Eya fikani.

Nabetha : Mwagona bwanji ndi odwalawa?

Nanyoni : Palibe kusitha kulikonse.

Nabetha : Mwamutani wathu mpaka chonchi, wasandukadi bwenzi la mphasa.

**Mafunso**

(I) Kodi ndi mtundu wanji wa malonje?

_______________________________________________(malikisi 1)

(II) Kodi Nabetha ndiyani munkhaniyi?

_______________________________________________(malikisi 1)

(III) Mawu oti **"bwenzi la mphasa"** akutanthauzanji?

_______________________________________________(malikisi 1)

(b) Kodi m'Malawi muno oyenda pansi amayenda mbali iti ya msewu?

____________________________________________________(malikisi 1)

(c) Tchulani njira **imodzi** yosamalira odwala?

____________________________________________________(malikisi 1)

**kupanga ziganizo**

5. Pangani ziganizo zomveka bwino ndi mawu awa:

(a) Puma

____________________________________________________________

____________________________________________________(malikisi 1)

(b) Ndekesha

____________________________________________________________

____________________________________________________(malikisi 1)

(c) Phu

____________________________________________________________

____________________________________________________(malikisi 1)

(d) Ngakhale

____________________________________________________________

____________________________________________________(malikisi 1)

(e) Kwa

____________________________________________________________

____________________________________________________(malikisi 1)

**GAWO D (malikisi 40)**

**Mafunso 6 mpaka 10**. Sankhani mitundu ya mawu omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo mziganizo zotsatirazi.

6. Ubwere nazo kuno.
   A. Muonjezi
   B. Mlumikizi
   C. Dzina
   D. Mneni
7. Onse adatenga mitolo yaikulu bwino.
   A. Mlumikizi
   B. Muonjezi
   C. Mlowam'malo
   D. Mperekezi
8. Ogo! Ufa wanga wataika.
   A. Dzina
   B. Mfotokozi
   C. Mvekero
   D. Mfuwu
9. Mphaka ali pa mpando.
   A. Mperekezi
   B. Mlumikizi
   C. Mneni
   D. mfotokozi
10. Aliyense apereke maganizo ake.
   A. Mneni
   B. Mlowamalo
   C. Dzina
   D. Mperekezi

**Mafunso 11 mpaka 15.** Sankhani zazimuna za mawu omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo m'ziganizo zotsatirazi.

11. Amayi akugulitsa thadzi pamtengo otsika.
   A. Tambala
   B. Tonde
   C. Chipsolopsolo
   D. Mdzakazi
12. Iwo aluza mfumukazi yawo.
   A. Mfumu
   B. Tatavyala
   C. Mumphwa
   D. Phungu
13. Mdzakazi wanga wapita kuchigayo.
   A. Mthoni
   B. Mpongozi
   C. Wakunjira
   D. kapolo
14. Iwo akwatira chumba.
   A. Mfuleni
   B. Gojo
   C. Mkwati
   D. Bambo
15. Nkhosa zakwathu zaswa.
   A. Mtheno
   B. Tonde
   C. Mzambwe
   D. Mphulu

**Mafunso 16 mpaka 20.** Sankhani mawu ofanana m'matanthauzo ndi mawu omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo mziganizo zotsatirazi.

16. Iwo adachita mphumi.
   A. Tsoka
   B. Mtendere
   C. Mwayi
   D. Phuma

17. Malita adadzuka ali bwamuswe.
   A. Maliseche
   B. Poyerayera
   C. Likuswa mtengo
   D. Ovala

18. Dzulo tidali ndi danga.
   A. Mwayi
   B. Tsoka
   C. Dothi
   D. Mpata

19. Agalu alumana minofu.
   A. Fupa
   B. Minyewa
   C. Mwazi
   D. Mponera

20. Uve ndiwosafunika pasukulu pano.
   A. Utchisi
   B. Ukhondo
   C. Kumbava
   D. Ulemu

**Mafunso 21 mpaka 25**. Perekani msintho yoyenera ya aneni omwe ali ndi mzere kunsi kwawo mziganizo zotsatirazi.

21. Mbuzi yadyedwa ndi mkango.
   A. Wochitidwa
   B. Wochititsitsa
   C. Wochita
   D. Wochitirana

22. Namwali wa mwano uja wapandwa.
   A. Wotsutsa
   B. Wam'chibisira
   C. Wobwerezabwereza
   D. Wonyazitsa

23. Yohane aphikira amayi nsima.
   A. Wochititsitsa
   B. Wochitira
   C. Wochitidwa
   D. Wochitirana

24. Ophunzira amatula pepala.
   A. Wotsutsa
   B. Wochititsa
   C. Wochitirana
   D. Wapoyera

25. Aphunzitsi ambiri amajombajomba kuntchito.
   A. Wapoyera
   B. Wam'chibisira
   C. Wochitirana
   D. Wobwerezabwereza

**Mafunso 26 mpaka 30.** Sankhani magulu a mayina omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo mziganizo zotsatirazi.

26. Ndege yafika nthawi yabwino.
   A. U-, Ma-
   B. I-, Zi-
   C. Chi,- Zi-
   D. Mu,- A-

27. Mwana waswa dzira.
   A. U-, Ma-
   B. Ka-, Ti-
   C. Mu-, Mi-
   D. Li-, Ma-

28. Chipewa chili kumutu.
   A. Mu-,Mi-
   B. Mu-,A-
   C. Ku-, Ma-, Mu-
   D. Ku + tsinde la m'neni

29. Tianapiye tonse tafa.
    A. Ka-,Ti-
    B. Chi-, Zi-
    C. Mu-, A-
    D. U-, Ma-
30. Ukapereke chakudya ku gowero.
    A. I-, Zi-
    B. Ka-, Ti-
    C. Chi-,Zi-
    D. Mu-,Mi-

**Mafunso 31 mpaka 35.** Sankhani mitundu ya afotokozi omwe ali ndi mzere kunsi kwawo mziganizo zotsatirazi.

31. Zinthu zomwe wandipatsa ndi izi.
    A. Wagwirizano
    B. Waumwini
    C. Woloza
    D. Wofunsira
32. Nkhuku izo ndi zawo.
    A. Wadzina lakelake
    B. Wotsimikiza
    C. Wotsindikiza
    D. Woloza
33. Iwo avala duku lachikasu.
    A. Waumwini
    B. Wamaonekedwe
    C. Wamakhalidwe
    D. Wochuluka
34. Ophunzira asanu ndi omwe alephera.
    A. Woloza
    B. Waumwini
    C. Wochuluka
    D. Wowerenga
35. Ng'ombe zathu zasowa.
    A. Waumwini
    B. Oloza
    C. Wadzina lakelake
    D. Wochuluka

**Mafunso 36 mpaka 40**. Sankhani mawu oyenera kutsiriza mikuluwiko yotsatirayi.

36. Zaku mzinda_____________.
    A. Safunsa
    B. Sasankha
    C. Sakana
    D. Saulula
37. Ndafulumira adasiya _____________m'khola.
    A. Bokho
    B. Tonde
    C. Chingwe
    D. Chifuyo
38. Kwaweni kudyetsa nthanga ___________nulifuna.
    A. Chimanga
    B. Mtedza
    C. Dzungu
    D. Chinangwa
39. _______________adafera mchenga woyera.
    A. Madoli
    B. Madolo
    C. Msomba
    D. Fulu
40. Aonenji adapha mvuwu_________________.
    A. M'mono
    B. Chavi
    C. Mfuti
    D. Uta

**Mafunso 41 mpaka 45**. Sankhani chiganizo chomwe chili ndi zizindikiro zoyenera za m'kalembedwe.

41.(A) Kodi munthu? sacheza ndi mfumukazi wake!
(B) Kodi? munthu sacheza ndi mfumukazi wake.
(C) Kodi munthu, sacheza ndi mfumukazi wake?
(D) Kodi munthu sacheza ndi mfumukazi wake?

42.(A) Anaphiri apita kumsika.
(B) anaphiri apita kumsika.
(C) anaphiri apita, kumsika.
(D) Anaphiri, apita kumsika.

43.(A) Ha, kaledi silibwerera.
(B) Ha kaledi silibwerera.
(C) Ha! Kaledi silibwerera.
(D) "Ha!" kaledi silibwerera.

44.(A) Iwo anati, "Timakonda kusambira".
(B) Iwo anati timakonda kusambira.
(C) Iwo anati; Timakonda kusambira.
(D) Iwo anati, timakonda, kusambira!

45.(A) Wophunzira yemwe wabwera mofulumira ndi Tawina.
(B) Wophunzira yemwe wabwera mofulumira ndi tawina.
(C) Wophunzira, yemwe wabwera mofulumira ndi Tawina.
(D) Wophunzira yemwe, wabwera, mofulumira ndi Tawina.

**MAFUNSO ATHERA PANO**